# Maphunziro a m'Baibulo

Bible studies

# Umoyo wa Elisa

1. Elisa afurukitsa Mafuta a mkazi wamasiye
2. Elisa ku Sunemu
3. Mkazi wa ku Sunemu ndi mwana wace
4. Madalitso
5. Nkhondo
6. Aaramu alangidwa ndi khungu ku Dotana

# 1. Elisa afurukitsa mafuta a mkazi wamasiye

**2 Mafumu 4.1-7**

1 Ndipo wina wa akazi a ana a aneneri anapfuula kwa Elisa, ndi kuti, Mnyamata wanu, mwamuna wanga wafa; mudziwa kuti mnyamata wanu anaopa Yehova; ndipo wafika wamangawa kunditengera ana anga awiri akhale akapolo ace.

2 Ndipo Elisa anati kwa iye, Ndikucitire ciani? undiuze m'nyumba mwako muli ciani? Nati, Mdzakazi wanu alibe kanthu m'nyumba, koma mtsuko wa mafuta.

3 Pamenepo anati, Kabwereke zotengera kwina kwa anansi ako onse, zotengera zopanda kanthu, zisakhale pang'ono.

4 Nulowe, uudzitsekere wekha ndi ana ako amuna ndi kutsanulira m'zotengera zonsezi, nuike padera zodzalazo.

5 Pamenepo anamcokera, nadzitsekera yekha ndi ana ace amuna; iwo namtengera zotengerazo, iye namatsanulira.

6 Ndipo kunali, zitadzala zotengera, anati kwa mwana wace, Nditengere cotengera cina, Nanena naye, Palibe cotengera cina. Ndipo mafuta analeka.

7 Pamenepo anadza, namfotokozera munthu wa Mulungu. Nati iye, Kagulitse mafuta, ukabwezere mangawa ako, ndi zotsalapo zikusunge iwe ndi ana ako.

**Mafunso**

1. Kodi mkazi anali ndi bvuto lotani kulingana ndi ndime ya 1?
2. Kodi Elisa anati ciani kwa iye? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Ndi ciani cimene cinacitika pamene mkazi anaika mafuta ake mutsuko? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi ana ake anatha kukhala ndi iye? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Mulungu amathandiza ngakhale masiko ano. Kodi mukhulupirira ici? Kodi mumafunsa thandizo la Mulungu?

**Sewero**

Pezani mau onse kukapeza yankho

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| M | T | S | U | K | O |
| I | A | N | A | W | M |
| N | M | F | U | A | L |
| A | B | M | U | Y | N |
| I | U | N | G | T | U |
| C | I | Z | A | K | M |

NYUMBA
MAFUTA
MTSUKO
MAU
MKAZI
MWANA
CIANI

**M.......................................**

## 2. Elisa ku Sunemu

**2 Mafumu 4.8-17**
8 Ndipo linafika tsiku lakuti Elisa anapitirira kumka ku Sunemu, kumeneko kunali mkazi womveka; ameneyo
anamuumiriza adye mkate. Potero pomapitirako iyeyu, adafowapa, mbukirako kukadya mkate.
9 Ndipo mkaziyo anati kwa mwamuna wace, Taona, tsopano ndidziwa kuti munthu uyu wakupitira pathu
pano cipitire ndiye munthu woyera wa Mulungu.
10 Timmangire kacipinda kosanja, timuikirenso komweko kama, ndi gome, ndi mpando, ndi coikapo nyali;
ndipo kudzatero kuti akatidzera alowe m'mwemo.
11 Ndipo linadza tsiku lakuti anafikako, nalowa m'cipinda cosanja, nagona komweko.
12 Nati kwa Gehazi mnyamata wace, Itana Msunemu uja. Namuitana, naima mkaziyo pamaso pace.
13 Ndipo anati kwa iye, Ufunse mkaziyu tsopano, kuti, Taona watisungira ndi kusamalira uku konse; nanga
tikucitire iwe ciani? Kodi tikunenere kwa mfumu, kapena kwa kazembe wa nkhondo? Koma anati, Ndikhala
ine pakati pa anthu a mtundu wanga.
14 Pamenepo anati, Nanga timcitire iye ciani? Nati Gehazi, Zedi alibe mwana, ndi mwamuna wace
wakalamba.
15 Nati, Kamuitane. Namuitana, naima pakhomo mkaziyo.
16 Ndipo anati, Nyengo yino caka cikudzaci udzafukata mwana wamwamuna. Koma anati, lai, mbuyanga,
munthu wa Mulungu, musanamiza mdzakazi wanu.
17 Ndipo mkaziyo anaima, naona mwana wamwamuna nyengo yomweyo caka cimene cija Elisa adanena
naye.

**Mafunso**

1. Kodi Elisa anadya mkate m'malo oti? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi mkazi ndi mwamuna wake anamkonzekera ciani kwa Elisa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Elisa analonjeza ciani m'malo mwa Mulungu kwa mkazi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Ndi cifukwa ciani Mulungu analonjeza lonjezo iri kwa mkazi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi mumasamalira anthu amene amakonda Mulungu?
6. Kodi mkazi anati ciani pamene anamva lonjezo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Mulungu anakwaniritsa cimene analonjeza?
8. Kodi Mulungu amakwaniritsabe malonjezo ake? Kodi mudziwako lonjezo mwa Baibulo?

### Sewero

Pezani mau onse

| | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| K | W | F | V | A | K | Y | G | Z |
| E | A | S | T | I | N | Y | G | X |
| L | K | A | U | M | Z | A | F | I |
| I | A | V | D | M | K | A | W | N |
| S | L | Q | H | N | E | A | K | M |
| A | A | E | R | T | I | M | T | M |
| H | M | U | E | J | V | P | U | E |
| I | B | T | P | I | L | R | I | J |
| P | A | I | Z | A | H | E | G | C |

| | |
|---|---|
| Sumemu | Mkazi |
| Mwana | Elisa |
| Mkate | Cipinda |
| Gehazi | Wakalamba |

## 3. Mkazi wa ku Sunemu ndi mwana wace

**2 Mafumu 4.18-37**

18 Ndipo atakula mwanayo, linadza tsiku lakuti anaturuka kumka kwa atate wace, ali kwa omweta tirigu.

19 Natikwa atate wace, Mutu wanga, mutu wanga! Pamenepo anati kwa mnyamata, Umnyamule umuke naye kwa amace.

20 Namnyamula, napita naye kwa amace. Ndipo anakhala pa maondo ace kufikira usana, namwalira.

21 Ndipo anakwera, namgoneka pa kama wa munthu wa Mulungu, naturuka, namtsekera.

22 Naitana mwamuna wace, nati, Nditumizire mmodzi wa anyamata ndi buru mmodzi, kuti ndithamangire kwa munthu uja wa Mulungu, ndi kubweranso.

23 Ndipo anati, Ulikumuka kwa iye lero cifukwa ninji? ngati mwezi wakhala, kapena: mpa sabata? Koma anati, Kuli bwino.

24 Pamenepo anamangirira buru mbereko, nati kwa mnyamata wace, Kusa, tiye; usandilezetsa kuyendaku, ndikapanda kukuuza.

25 Potero anamuka, nafika kwa munthu wa Mulungu ku phiri la Karimeli. Ndipo kunali, pakumuona munthu wa Mulungu alinkudza kutali, anati kwa Gehazi mnyamata wace, Tapenya, suyo Msunemu uja;

26 uthamange tsopano kukomana naye, nunene naye, Muli bwino kodi? mwamuna wanu ali bwino? mwanayo ali bwino? Ndipo anati, Ali bwino.

27 Ndipo pofika kwa munthu wa Mulungu kuphiri anamgwira mapazi. Ndipo Gehazi anayandikira kuti amkankhe; koma munthu wa Mulungu anati, Umleke, pakuti mtima wace ulikumwawa; ndipo Yehova wandibisira osandiuza ici.

28 Ndipo mkaziyo anati, Ngati ndinapempha mwana kwa mbuyanga? Kodi sindinati, Musandinyenga?

29 Pamenepo anati kwa Gehazi, Udzimangire m'cuuno, nutenge ndodo yanga m'dzanja lako, numuke; ukakomana ndi munthu usamlankhule; akakulankhula wina usamyankhe; ukaike ndodo yanga pankhope pa mwanayo.

30 Koma mace wa mwana anati, Pali Yehova, pali inunso, ngati nkukusiyani. Ndipo ananyamuka, namtsata.

31 Nawatsogolera Gehazi, naika ndodo pankhope pa mwanayo; koma mwanayo analibe mau, kapena kusamalira. Motero anabwerera kukomana naye, namuuza kuti, Sanauke mwanayo.

32 Ndipo pamene Elisa analowa m'nyumba, taonani, mwanayo ngwakufa, adamgoneka pakama pace.

33 Nalowa Elisa, nadzitsekera awiriwa, napemphera kwa Yehova.

34 Nakwera, nagona pa mwanayo ndi kulinganiza pakamwa pace ndi pakamwa pace, maso ace ndi maso ace, zikhato zace ndi zikhato zace, nadzitambasula pa iye, ndi mnofu wa mwana unafunda.

35 Pamenepo anabwera nayenda m'nyumba, cakuno kamodzi, cauko kamodzi; nakwera, nadzitambasuliranso pa iye; ndi mwana anayetsemula kasanu ndi kawiri, natsegula mwanayo maso ace.

36 Pamenepo anaitana Gehazi, nati, Kaitane Msunemu uja, Namuitana. Ndipo atalowa kuli iye, anati, Nyamula mwana wako.

37 Iye nalowa, nagwa pa mapazi ace, nadziweramitsa pansi; nanyamula mwana wace, naturuka.

**Mafunso**

1. Ndi ciani cimene cinacitika kwa mwana wa mkazi m'Sunemu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Kodi mkazi anauza mwamuna wake cimene cidacitika? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Elisha anabwera m'nyumba ya mkazi. Kodi anacita ciani coyamba? Werengani ndime 33.
4. Kodi tingaphunzire ciani m'Elisa? Kodi mumapemphera kangati kwa Mulungu?
5. Kodi Elisa anacita ciani pambuyo pa kuphempera? Werengani ndime 34 ndi 35.
6. Kodi mwana anakhalanso ndi moyo? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi ndi Elisa amene anaukitsa mwana kapena Mulungu?

# 4. Madalitso

**2 Mafumu 4.38-44**

38 Ndipo Elisa anabwera ku Giligala, koma m'dzikomo munali njala; ndi ana a aneneri anali kukhala pansi pamaso pace; ndipo anati kwa mnyamata wace, Ika nkhali yaikuruyo, uphikire ana a aneneri.
39 Naturuka wina kukachera ndiwo kuthengo, napeza conga ngati mpesa, nacherapo zipuzi kudzaza m'pfunga mwace, nadza, nazicekera-cekera m'nkhali ya cakudya, popeza sanazidziwa.
40 Pamenepo anagawira anthu kuti adye. Koma kunali; pakudya cakudyaco, anapfuula nati, Munthu wa Mulungu, muli imfa m'nkhalimo. Ndipo sanatha kudyako.
41 Pamenepo anati, Bwera naoni ufa. Nathira m'nkhalimo; nati, Gawirani anthu kuti adye. Ndipo m'nkhalimo munalibe cowawa.
42 Ndipo anadza munthu kucokera ku Baala Salisa, nabwera nayo mikate ya zipatso zoyamba kwa munthu wa Mulungu, mikate ya barele makumi awiri, ndi ngala zaziwisi za tirigu zosaomba. Ndipo anati, Uwapatse anthu kuti adye.
43 Koma mnyamata wace anati, Ciani? ndig awire amuna zana ici kodi? Koma anati, Uwapatse anthu kuti adye; pakuti atero Yehova, Adzadya nadzasivako.
44 Potero anawagawira, nadya, nasiyapo, monga mwa mau a Yehova.

**2 Mafumu 6.1-7**

1 Ndipo ana a aneneri anati kwa Elisa, Taonani tsono, pamalo tikhalapo ife pamaso panu paticepera
2 Mutilole tipite ku Yordano, tikatengeko, ali yense mtengo, tidzimangire malo komweko, tikhalepo, Nati, Mukani.
3 Ndipo wina anati, Mulole mupite nafe anyamata anu. Nati, Ndidzamuka.
4 Namuka nao, nafika ku Yordano, iwo natema mitengo.
5 Ndipo wina analinkudula mtengo nkhwangwa inagwa m'madzi; ndipo anapfuula, nati, Kalanga ine mbuyanga! popeza ojobwereka.
6 Nati munthu wa Mulungu, Yagwera pati? Namuonetsapo yagwera. Pamenepo anadula kamtengo, nakaponya pomwepo, nayandamitsa nkhwangwayo.
7 Nati, Katole. Natambasula dzanja lace, naitenga.

**Mafunso**

1. Ndi bvuto lotani limene anapeza pambuyo pa kuika zipuzi mu mbiya?
2. Kodi Elisa anacita ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi ciani cinacitika atacita tero Elisa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Ndi ciani cimene cinacitika ndi mikata kulingana ndi ndime za 43 ndi 44?
5. Kodi ndi ciani cimene cinacitika ndi kunkhwangwa? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi cinatheka bwanji kuti citsulo cinayandama? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Elisa analandira madalitso ambiri kucokera kwa Mulungu. Kodi mumalandiranso madalitso? Ngati inde, ndi madalitso otani?

**Sewero**

Pezani mau onse kukapeza yankho

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| E | M | U | A | M |
| A | L | D | A | B |
| L | I | I | T | E |
| I | S | O | S | S |
| N | J | A | L | A |
| E | I | M | F | A |

MAU MBESA
ELISA NJALA
IMFA INE

.............................................................

## 5. Nkhondo

**2 Mafumu 6.8-18**

8 Ndipo mfumu ya Aramu inalinkucita nkhondo ndi Israyeli, nipangana ndi anyamata ace, kuti, Misasa yanga idzakhala pakuti pakuti.
9 Ndipo munthu wa Mulunguyo anatuma mau kwa mfumu ya Israyeli, ndi kuti, Mucenjere musapite pakuti, popeza Aaramu alikutsikira uko.
10 Pamenepo mfumu ya Israyeli inatumiza kumene munthu wa Mulungu anamuuzako ndi kumcenjeza; nadzisunga osapitako, kawiri kawiri.
11 Koma mtima wa mfumu ya Aramu unabvutika kwambiri pa icico, naitana anyamata ace, nanena nao, Kodi simudzandiuza wina wa ife wobvomerezana ndi mfumu ya Israyeli ndani?
12 Nati mmodzi wa anyamata ace, lai, mbuye wanga mfumu; koma Elisa, mneneriyo ali ku Israyeli, ndiye amafotokozera mfumu ya Israyeli mau muwanena m'kati mwace mwa cipinda canu cogonamo.
13 Nati iye, Kamuoneni komwe ali; ndikatume munthu kumtenga. Ndipo anamuuza kuti, Ali ku Dotana.
14 Pamenepo anatumizako akavalo ndi magareta ndi khamu lalikuru, nafikako usiku, nauzinga mudziwo.
15 Ndipo atalawirira mamawa mnyamata wa munthu wa Mulungu, naturuka, taonani, khamu la nkhondo linazinga mudzi ndi akavalo ndi magareta. Ndi mnyamata wace ananena naye, Kalanga ine, mbuye wanga! ticitenji?
16 Nati iye, Usaopa, pakuti okhala pamodzi ndi ife acuruka koposa aja okhala pamodzi ndi iwo.
17 Ndipo Elisa anapemphera, nati, Yehova, mumtsegulire maso ace kuti aone. Pamenepo Yehova anamtsegulira maso mnyamatayo, napenya iye, ndipo taonani, paphiripo panadzala ndi akavalo ndi magareta amoto akumzinga Elisa.
18 Ndipo atatsikira pali iye, Elisa anapemphera kwa Yehova, nati, Mukanthe mtundu uwu ucite khungu. Ndipo iye anawakantha, nawacititsa khungu, monga mwa mau a Elisa.

**Mafunso**

1. Kodi ndani amene anamenyera Aisrayeli? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
2. Ndi cifukwa ciani mfumu ya Aramu anatuma ankhondo ambiri kwa Dotana kuti agwire Elisa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Mnyamata wa Elisa anaona ankhondo poyamba. Kodi anaopa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi Elisa anaopa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Ndi cifukwa ciani Elisa sanaope? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Elisa anaphempera ciani kulingana ndi ndime ya 17?
7. Kodi mnyamata anaona ciani pambuyo pa phempero iri? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
8. Mulungu amateteza ana ake. Kodi mumamuphempa citetezo cake tsiku lirilonse?

## 6. Aaramu alangidwa ndi khungu ku Dotana

**2 Mafumu 6.18-23**

18 Ndipo atatsikira pali iye, Elisa anapemphera kwa Yehova, nati, Mukanthe mtundu uwu ucite khungu.
Ndipo iye anawakantha, nawacititsa khungu, monga mwa mau a Elisa.
19 Ndipo Elisa ananena nao, Ngati njira ndi iyi? ngati mudzi ndi uwu? munditsate ine, ndidzakufikitsani kwa
munthu mumfunayo; nawatsogolera ku Samariya.
20 Ndipo kunali, pakufika ku Samariya, Elisa anati, Yehova, muwakanganulire awa maso kuti aone.
Nawakanganulira Yehova maso ao, naona iwo, ndipo tapenyani, ali pakati pa Samariya.
21 Niti mfumu ya Israyeli kwa Elisa pakuwaona, Atate wanga ndiwakanthe kodi, ndiwakanthe?
22 Nati, Musawakanthe; kodi mumakantha omwe mwawagwira ndi lupanga ndi uta wanu? apatseni mkate
ndi madzi adye namwe, namuke kwa mbuye wao.
23 Ndipo anwakonzera cakudya cambiri, nadya namwa iwo; nawauza amuke; namuka kwa mbuye wao.
Ndipo magulu a Aramu sanadzanso ku dziko la Israyeli.

**Mafunso**

1. Kodi Elisa anafunsa ciani kwa Mulungu kulingana ndi ndime ya?
2. Kodi Mulungu anayankha pemphero la Elisa? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Elisa anawapereka kuti asirikali? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
4. Kodi mfumu wa Israyeli anapha asirikali? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
5. Ndi cifukwa ciani mfumu wa Israyeli anaphe asirikali a Aaramu? Ndi m’ndime iti mwapeza yankho?
6. M’Baibulo tiwerenga: Kondanani nao adani anu (Mateyu 5.44). Kodi ici cithanthauza ciani?

**Sewero**

Pezani mau onse

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| A | R | A | M | U | P |
| E | M | S | P | M | O |
| U | S | I | K | U | T |
| H | Y | L | E | F | O |
| E | R | E | A | M | M |

ARAMU ELISA
MFUMU USIKU
MOTO IYE